



BWENZI
la USIKU



Director: Yolandé Korkie

E-mail: Yolande.korkie@crisisresponsenetwork.net

Website: www.crisisresponsenetwork.net

Tel: +27 (0) 21 9761465

BWENZI la USIKU TEAM

Illustrator: Huibrecht de Hart

E-mail: deharth2@gmail.com

Author: Maretha Maartens

E-mail: strydomsuster@gmail.com

Translators, Chichewa:

AnnaMarie de Klerk

E-mail: annamdeklerk1@gmail.com

Fletcher Chulenje

E-mail p/a: annamdeklerk1@gmail.com

Marlene Kaliko

E-mail: marlenekaliko@gmail.com

Hannah Phiri

E-mail c/o: marlenekaliko@gmail.com

Rhodess Abel

E-mail: rhodess@dalitsotrust.org

ISBN BWENZI la USIKU

Application submitted.



Read *BWENZI la USIKU* just like a book.

This PDF may display only one page at a time when you open it. But most of us want to read an online publication with two pages displayed side-by-side, just like a book.

If you have Adobe Reader (a free program for viewing PDFs) installed on your tablet, mobile phone or laptop, you can easily change the one page view to a two-page view.

This is how you do it:

Open the NIGHT FRIEND online PDF book in ADOBE READER.

If you see only one page, find **View** (right above HOME, TOOLS and the PDF title).

Click on **View**.

Then click on **Page Display**.

Choose the option: **Two Page View**.

That's it! Enjoy your book!



Bwenzi la Usiku





Sami akulota maloto ochititsa mantha ndithu.

Walephera kuturukamo.

M'maloto akewo, tizirombo toyambitsa nthenda
tikufanana ndi mmene timawonekera ndithu.

Tikuwoneka ngati timipira tating'ono tothilira mafuta.

Timipira tonse tiri ndi minga yambiri yofanana ndi
nkhanyanga.

Sami akuwona tizirombo toyambitsa nthenda ya Covid-
19 tochuruka, tiripo mazana mazana.

Polota, Sami wawona kuti tizirombo toyambitsa
nthenda tamamatira pa manja a Agogo ake aamuna.

Agogo ake aamuna akhudza china chake chimene
chinali ndi tizirombo tambiri toyambitsa nthenda.


Agogo akuyimba nyimbo

“Yesu andikonda ‘ne.

Amatero m'Bukumo.”

M'maloto akewo Sami akuwona kuti Agogo aamuna
akhudza dzanja la Agogo aakazi,

nawapempha Agogo aakazi, nati “Tiyeni, tiyimbe
limodzi”.



Agogo aakazi awafunsa Agogo aamuna “Kodi mwasamba m’manjamo?”

Agogo aamuna akuwayankha “Mphaka amanyambita mapazi ake.

Sindine mphaka.”

Tizirombo toyambitsa nthenda takakamiranso pa dzanja la Agogo aakazi.

Agogo aakazi sakudziwa kuti tiziromboto takakamira pa dzanja lawo, chifukwa tizirombo toyambitsa nthenda ntating’onong’onodi.



"AYETSI!" Agogo aamuna akuyetsemula. "Taleka mphuno yoyabwa!"

Mwina tizirombo toyambitsa nthenda tayamba kale kuchuruka mu timadontho tamadzi oturuka m'mphuno mwa Agogo aamuna.

"AYETSI!" Agogo aamuna ayetsemulanso.

M'maloto a Sami kuyetsemula kwa Agogo aamuna kukumveka ngati phokoso loopsya.

Timadonthoto ta m'mphuno mwa Agogo aamuna tagwera pa thebulo ndiponso pa mipando.

Tina tagweranso pa nkhope ya Agogo aakazi.

Ndipo Agogo aamuna akungofikisafikisa ndi kukhudza mphuno yawo.



Tizirombo toyambitsa nthenda sitithamanga kapena kujowajowa.

Tiribe miyendo, tiribenso maso, mapazi kapena pakamwa ayi.

Koma m'maloto ake Sami wamva bwino lomwe kuomba kwa timingaminga taketo timati khwi-khwi-khwiii.

Poomba khwi-khwi-khwiii, tanyadira

"Takupeza, nkhalamba iwe!"

Agogo aamuna sakudziwa kuti tizirombo toyambitsa nthenda tawalowa m'thupi.

Taombanso khwi-khwi-khwiii "Sami, thupi la Agogo ako aamuna ndi nyumba yathu tsopano!"



Sami akufunitsitsa akadafuula. Koma akulephera chifukwa ali m'tulo.

Ku sukulu ali yense adaphunzira za tiziromboti toyambitsa nthenda.

Timinga take ta tizirombo toyambitsa nthenda ya Covid-19 timaposa ubweya wa chiyabwe.

Timinga taketo timamamatira pa khungu lofewa la m'mphuno za anthu.

Khungu lofewa la m'mphuno za anthu ndi malo abwino oti tizirombo tidzikhazikikamo.

M'katikati mwa khungu lofewa la m'mphunomu, muli timagawo ting'onoting'ono timene tizirombo toyambitsa nthenda ya Covid-19 timafuna kuti tidziphathikemo kuti tiswane.

Tiziromboto tikalowa mu timagawo tating'onoting'ono timeneti, tikaswana mmenemo ndipo timafalikira msanga!

Timagawo tating'ono momwe tiziromboti taswaniranamo timaphulika. Tizirombo toswana tija timafalikira ndikukalowanso mkatikati momwemo mwa khungu lofewa la m'mphuno ndikuyambaso kuswana.

Sami akufuna kudzuka, koma walephera chifukwa akadalota.

Walepheleratu kudzuka.

Agogo aamuna apangitsa kuti tizirombo toyambitsa nthenda tiwagwere Agogo aakazi.

Posakhalitsa tizirombo timene timayambitsa nthenda ya Covid-19 tiswana ndi kufalikira mkatikati mwa khosi modutsira mpheya ndiponso mu mapapu mwa agogo onse awiri.



Mwadzidzidzi ku sukulu ya Sami ana khumi adayesedwa ndi kupezeka ndi tizirombo toyambitsa nthenda ya Covid-19.

Ena adatsokomola kwambiri ndiponso amatentha thupi.

Ena sadawoneke ndi zizindikiro zoti akudwala.

Mphunzitsi wamkulu adafotokozera kuti nthendayo ya Covid-19 yafalikiraso koma ulendo uno nthendayi singakhalitse nthawi yaitali.

Mpofunika kuti aliyese akakhale kunyumba kwao osayenda yenda monga

momwe adachitira

mu mwezi wa Malichi ndiponso Epulo.

Mphunzitsi wamkulu adafotokozeranso nati, “Nonsenu mwakhala mukudziwa kuti

kachirombo koipa koyambitsa nthendayi sikayenera kufalikira makamaka kwa

agogo athu ndi anthu odwaladwala.

Okhalamba ndi odwaladwala akagwidwa ndi nthendayi sangotsokomola ndi

kuyetsemula kokha.

Ena pakati pa akuluakulu amadwala modetsa nkhawa akakhudzidwa ndi nthenda ya Covid-19 yofalitsidwa ndi ananu.”

Izi ndizomwe zidawachitikira Amayi Sara.



Amayi Sara adayendetsa kasitolo ka zakudya kuseri
kwa mpanda wa matabwa.

Ankagulitsa mandazi okoma kwambiri.

Mdzukulu wawo, Yosefe, adangotsokomola pang'ono
podwala nthendayi.

Potsokomola m'nyumba ya Agogo wake aakazi,
sadavale nkomwe kansaru kophimbira pa mphuno ndi
pakamwa pake.

Potsokomola timadontho ta tizirombo toyambitsa
nthenda ya Covid-19 tidafalikira.

Tiziromboto tidayamba kukhazikika mu khungu lofewa
la m'mphuno ya Amayi Sara.

Pambuyo pake nthenda ya Covid-19 idalowanso mu
mapapu a Amayi Sara.

Adangodwala masiku anayi okha asanamwalire.

Kutsokomola kwa Yosefe kudatha kale kale, koma
akadapukwa Agogo wake aakazi usana ndi usiku.



Tawonani, m'mphuno mwa Agogo aamuna mwadzaza ndi tizirombo toyambitsa nthenda ya Covid-19!

Maloto ochititsa mantha amangopitirira mosalekeza.

Agogo aamuna akucheza ndi Agogo aakazi nati, “Tiyeni tiziyimbabe, kufikira mwezi utaturuka”.

Agogo aakazi agwedeza mutu wao nayankha, “Iyayi, sitifuna kudya chakudya chopsyeleza”.

Agogo aamuna ayankha moseka, “Chotsani chakudya pa mbaula”.

Agogo aakazi ayankha, “Lero tidyera zipalapasiro zokazinga za nkhuku. Mulibe njala?”

“Zipalapasiro zokazinga za nkhuku? Zoona?” Agogo aamuna ayamba alingalira. Kenaka agwedeza mutu wawo.

“Basiyani zipalapasiro za nkhukuzo. Ndifuna kuyimba kufikira mwezi utatuluka ndi kukwera kumtunda!”

M'maloto ochititsa mantha, agogo aamuna amangofikisafikisa mphuno yawo.

“Tizichotsa touluka topezeka mu chipinda chino.”
adandaula Agogo aamuna.

“Nchifukwa chake mphuno yanga ikuyabwabe”.



Sami akupfuula “Agogo aamuna! Agogo anga aakazi !”

Koma Agogo onse awiri sakumva kuitana kwake.

M'maloto oopsyawo Agogo aakazi akutsonyeza

chipalapasiro chonse cha nkuku m'kamwa mwawo.

Agogo aamuna akudandaula kuti atenthedwa.

Akutsegula chitseko.

Malotowa ndi oopsyadi.

Chogwirira cha chitseko chikuoneka chitakula

kwambiri. Chafanana ndi chimbale cha televishoni.

Chogwirira chachikulu cha chitseko chonse chadzala

ndi tizirombo toyambitsa nthenda ya Covid-19

tochokera m'manja a Agogo aamuna chifukwa sasamba

m'manja mwao.

Chifukwa nchiyani Agogo aamuna amakana kusamba

m'manjamo?

Chifukwa nchiyani amakana kuyetsemulira pa


kasukusuku?

Sami akuganizira, wina ayenera kuchitapo kanthu.
M'maloto akewo akuyesayesa atauluka,
koma m'malo mouluka wagwa pansu ndi kuthyola chala
chaku phazi.
Akufuula: kalanga ine, kalanga ine!





M'maloto akewo akuyesetsa kusambira
koma ng'ona ikumuyandikira ndi kumasambira naye
limodzi
ndipo kwatsala pang'onong'ono kuti Sami amire.



M'maloto akewo akuyesetsa kuthamanga,
koma Pusi wagona pa miyendo yake.

Pusi akulemera kwambiri ngati chotengera chachikulu
chodzala ndi mabuku.



M'maloto akewo akuyesanso kukuwa.

Koma khoswe akulowetsa m'kamwa mwake ubweya wambiri wa mphaka.

Ubweya wa mphaka! Ngwosanzitsa!

Khoswe akumuletsa mwaukali: "Sami, khala chete."

"Ndapsya mtima. Tamvera nyimbo yomwe akuyimba Agogo ako aamuna. Sindikondweretsedwa nayo."

Agogo ake aamuna a Sami akuyimba nyimbo yokhudza khoswe:

Khoswe wameta mpaka khoswe!

Khoswe walaula!





M'maloto oopsya Sami akuona kuti timapazi ta khoswe tadzala ndi tizirombo toyambitsa nthenda.

Khoswe wapsya mtima ndi Agogo aamuna chifukwa akuyimba za makhoswe.

Khosweyo akuwapaka Agogo aamuna tizirombo toyambitsa nthenda.

Khoswe akuyetsemula ndi kutsokomolera pa Agogo aamuna.

Alibe chifundo.

Akupanga zonsezi mwadala.

Sami akulira “Amayi! Thandizeni!”
 Sami akupitiliza kufuula: “Thandizeni. Thandizeni!”
 Pusi akujowa kumuchokera Sami pa miyendo yake.
 Tsopano Sami wamasuka kuti akhoza kusuntha miyendo.
 Sami akuvundukula zofunda zake.
 Mayi wake akuthamangila msanga kuchipinda chake, namufusa
 “Sami? Chavuta ndichiyani, Sami?”
 Pusi akulira miaau ndipo akudzuma molusa ndikudutsa molewa mayi wa Sami.
 “Ndiri pano!” Mayi wa Sami akulankhulanso “Ndiri pano, mnyamata wanga”.
 Mayi wake akusuntha kuti apeze nyale imene imakhala pa kathebulo ka thabwa pafupi ndi bedi lake. Mayi wa Sami akuiyatsa nyaleyo.
 Mayi wake akumufunsa “Kodi walota maloto ochititsa mantha?”
 Sami walephera kulankhula momveka. “Agogo aamuna adzadwala.
 Sasamba m'manja mwawo.
 Khoswe woipa ali ndi tizirombo toyambitsa nthenda”
 Sami akadalirabe:
 “Khoswe woipa uja adawapaka Agogo aamuna tizirombo toyambitsa nthenda!”
 “Mayi wa Sami adati: "Mwa mwayi wangolota maloto."
 "Wina aliynse amadziwa kuti khoswe amangotola nyungu ndi kena kali konse kamene tonsefe timakakondanso. Koma khoswe sangapakire wina aliynse tizirombo toyambitsa nthenda ya Covid, yayi. "



Mayi wa Sami watopa kwambiri sanapumule chichokere ku ntchito.

Komabe akusankha kukhala naye ndipo adzifunditsa ndi zofunda za Sami.

Akumufungatira ndipo Sami akumva ngati mwanapiye akabisala m'kwapa mwa make.

Mayi wake akumutonhoza nati, “maloto ako ndi oopsyadi!”

Sami akuvomera. “Tizirombo toyambitsa nthenda ya Covid-19 tidawasinjilira Agogo aamuna. Tidafuula kuti

Takupeza, nkhalamba iwe!”

Mayi wake akumufungatira Sami.

Akumufotokozera momulimbitsa mtima kuti,

“Agogo aamuna adandiyimbira dzuwa lisanalowe.

Kumeneko onse ali bwino.


Taganizira kodi madzulo ano adadyera chiyani?”

Sami akuyankha moyerekeza, “Kodi Mayi, adadyera mpiru wotendera?”

Mayi wake akuvomera,

“Inde, Agogo aakazi adawaphikira nsima ndi mpiru wotendera komanso

nyemba. Ndiwo zonsezo Agogo aamuna adathyola kudimba kwawo”.





Sami akumva mmene
mng'nono wake Chikondi
wadzukira m'chipinda
chake.

Mayi wake wangokhala du!
Mai wake akumunong'oneza
Sami, “Tiyeni, asanalire
timuyimbire nyimbo
mng'ono wakoyo”.

Sami akuyambiratu

kuyimba “Tonthola Chikondi, tonthola”.

Mayi wake akuyimbanso, “Chikondi, tonthola, tonthola,
Chikondi!”

Chikondi wakhala chete.

Akusekerera.

Chikondi amasekerera motere Pusi akakhala naye pa
bedi lake ndikumasewela naye.

Sami akudzuka msanga, nathamangira ku chipinda cha
Chikondi.

Pusi akukhaladi pa bedi la Chikondi, nagiligisha tsaya la
Chikondi ndi phazi lake.

Mayi wake wa Sami akumutsatira.

Akumunyamula Pusi.

Sami akudzipereka msanga nati, “Mayi, Pusi akhoza kudzagona pa bedi langa”.

Mayi wake akuyankha, “Iyayi, adzatisautsa.

Pusi ayenera kuturuka ndi kukasakasaka”.

Sami akudandaula, napempha, “Mayi, mumdima ndimachita mantha. Kodi mungalole kuti Pusi akhale nane pafupi?”

Mayi wake akuyankhanso, “Iyayi, tonse tizigona tsopano. Tigone modekha kufikira ataweruka Bambo wako kuntchito ndi kudzatipeza.”



Mayi akutsegula chitseko ndi kumuponya panja Pusiyo.

“Tiye, tiye Sami. Bwerera ku bedi lako.”

Sami akuyesanso kudandaula. “Mdimu umandiopsya Mayi.”

“Chabwino, usazime nyale. Lingalira za zinthu zabwino.”

“Monga chiyani, Mayi?”

Mayi wake akukoka mtima. “Kali konse!”

Mayi wake akuwoneka wotopa kwambiri.

Akuzimitsa nyale ya pa kathebulo kali pafupi ndi bedi la makolo ake.

“Sami, kagone!”



Sami akupita ku chipinda chake.

Akukasuzumira pa kazenela ka chipinda chake.

Pusi akukhala pa mpanda wa matabwa. Kuseri kwake,
mwezi waukulu wofiirila ukuwoneka.

Mileme yambiri ikuuluka pamalopo.

Milemeyo ikupanga phwando mumtengo wa mango.

Pusi akukonzekera kukagwira mleme.

Sami akulingalira kuti Pusi mleme si chakudya chako
choyenera.

Koma Sami asanachenjeze Pusi kuti, “Usayelekeze
kugwira mleme!” Pusi akuyetsemula kwambiri .

Tsiku lina timadontho taketo tidagwera phala la Chikondi.

Timadontho ta kuyetsemula kwa Pusi, tikuwoneka ngati changululu mu kuunika kwa mwezi.



Mayi adachotsa phala la Chikondi namudzudzula Pusi:
“Iyayi, Pusi, iyayi!
Ukapitirira kutero tidzayenera kukuvekanso kansaru kotchinga mphuno ndi pakamwa.”


Mayi akufotokozera kuti timadontho tamalovu ndilo gwero lenileni la kachirombo koyambitsa nthenda ya Covid-19.

Ana akangodwala pang’ono, nayetsemula, mu kuyetsemula kwawoko mumapezekabe tizirombo toyambitsa nthenda ya Covid-19 tosawonekera mu timadontho tamalovu.

Ana akangodwala pang’ono, nayimba kapena kulankhula, mu kuyimba kapena kulankhula kwawo,

mumapezekabe tizirombo toyambitsa nthenda ya Covid-19 tosawonekera mu timadontho tamalovu.

Ana akatsokomola, ngakhale pang'onong'ono, timadontho todzala ndi tizirombo, timaturuka pa kamwa pawo.



Timadontho timene tiri ndi tizirombo tosawonekera toyambitsa nthenda tikamagwera pa zogwirira zitseko, zofungulira ndiponso pa mafoni, timatha kudwalitsa kwambiri anthu.

Nchifukwa chake onse ayenera kuvala kansaru kotchinga mphuno ndi pakamwa akamasakanizana ndi anthu kunja kwa nyumba zawo.

Pusi akuyetsemulanso nasowa mwadzidzidzi.

Wajowa pa mpanda wa matabwa.

Wafika kuseri kwa mpanda mu msika wa malonda.

.

Ku msika wa malonda anthu ankasewera mpira.
Ku msika wa malonda ndikomwe abambo a dzitho
ankaphunzitsa anyamata kumenya mkhonya.
Ku msika wa malonda agalu ankathamangathamanga.
Ku msika wa malonda kunkapezeka timasitolo tambiri.
Mu timasitoloti munkapezeka malonda osiyanasiyana:
mango ndi nzimbe
zipeso
mpunga ndi ufa
mandazi
zipalapasiro zokazinga
ndiwo za masamba
osiyanasiyana
masiwiti ndi zakumwa
sopo ndi ndowa
zikhwama
zovala ndi nsapato.
Ku msika wa malonda
Mayi Sara ankagulitsa
mandazi:mandaziwo
adali okoma kopambana
pa dziko lonse lapansi.



Koma ku bwalo la msika kulibe anthu tsopano
chifukwa onse ayenera kukhala pa khomo
kuti ana aja ophunzira ku sukulu ya Sami amene
akudwala
ayambe achira
Sami akulingalira, ndine wokhumudwa chifukwa cha
kachirombo koyambitsa nthenda.
Ndapsya mtima kwambiri.
Amayi okha akumapita ku msika wa malonda tsopano.
Amavala kansaru kotchinga mphuno ndi pakamwa
ndipo amabwelerako msanga.
Mayi wa Sami amapita pa Chiwiri paliponse.
Pa tsikulo sakolopa ku chipatala kapena kutsuka
masinki
Mayi sakukwanitsanso kugula mandazi.
Zakumwa zadula kwambiri.
Mayi wa Sami amagula zofunika zochepa ndipo chiri
chonse chiyenera kusamalidwa.

Sami wangoima pa kazenala ka chipinda chake
ndikuyang'ana kunja.

Akulakalaka nyengo yabwino pamene msika wa
malonda udali ndi zosangalatsa.

Akulakalaka

zipalapasiro za nkhuku

zokazinga

ndi mandazi ndipo

akuwapukwa Mayi

Sara.

Akulakalaka kusewera

mpira ndi kumenya

mkhonya

ndipo akusowanso

anzake.

Ankakhallirana bwino

wina ndi mnzake.

Sami akulingalira, Ndine wokhumudwa chifukwa cha

kachiroombo koyambitsa nthenda.

Ndipo ndiri ndi mantha.



Nyale yake ya pa kathebulo yazima.

M'chipinda chonse mwada bii.

Chiri chonse chadzala ndi mdima.

Sami akulingalira kuti nthawi yeniyeni yoopsya
imakula pakati pa usiku.





Sami akuphukwa Bambo wake
amene amagwira ntchito ya ulonda ku sukulu ya
primary.

Usiku amayang'nira bwalo lonse la ku sukulu.

Bambo wake akadangokhala womasuka monga kale.

Masiku ano Bambo akangofika pakhomo,
amamuletsa Sami: “Taima, taima, Sami! Ndiyambe
ndasamba.

Usandikhudze tsopano.”

Ngakhale Mayi amatiletsa momwemo
akafika pa khomo kuchokera ku ntchito.



Sami akumva kuwawa

pakatikati pa chifuwa chake.

Kuwawaku ndi chifukwa cha Agogo aamuna ndi Agogo
aakazi.

Akuwapukwa.

Kupukwa kwake kufanana ndi bala latsopano

ngati wadziphweteka

pakatikati pa chifuwa chake.

Zonse zada bii.

Ngati mdima.

Sami akulingalira kuti pakati pa usiku ndi nthawi

yomvetsetsa

kuunguluma ndi

chisoni.



Sami akukalowanso pang'onopang'ono m'bedi lake.
Mwezi ukubisala kuseri kwa mtambo.
Pusi akadayendayenda pa yekha kuseri kwa mpanda wa
matabwa.
Usiku wonse Bambo akutetezera anthu ndi malo.
Ndi ntchito yawo.
Sami akumva mmene Chikondi akuyamwira kena kake.
Mayi akutembenukatembenuka. Mayi wake asanagone
ngakhale watoperatu. Popeza tulo tamusowa, Sami
wamva bwino lomwe zonsezi.

Zonse zada bii,

Ngati mdima.


Sami akulingalira: pakati pa usiku
ndi nthawi yondipangitsa
kuunguluma.

Sami akutembenukatembenuka
chimodzimidzi Mayi wake.

Mwina ndi bwino kukhala tsonga? Mayi wake
akumvanso kuti Sami akusowa mtendere.

“Sami,” akumulankhulira motsitsa mawu “uziganizira
za nkhani yosangalatsa imene Agogo aamuna
amakufotokozera. Udzalimbikitsidwa bwino.”





Sami akulingalira
mumdima momwemo kuti
nkhani yosangalatsa
koposa imene Agogo
aamuna adamufotokozero
ndi nkhani ya Bwenzi la
usiku.

Akukumbukira kuti
adakhala pa bondo la
Agogo aamuna.

Nthawi zonse Agogo
aamuna akamafotokozero

nkhani, umakhala pa bondo lawo.

Nkhani ya Bwenzi la usiku imene Agogo aamuna
amafotokozero ndi nkhani yosangalatsa kupambana
nkhani zina zonse.

Sami akufungatira mtsamilo wake.

Nthawi yomweyo Sami akufanizira kuti mtsamilo
wafundako mofanana ndi thupi la Agogo aamuna.

Ndi chimodzimodzi ngati akumvera liu la Agogo
aamuna pamene akamufotokozero nkhani mumdima bii:

“Sami, mnyamata wanga, kale kalelo
anthu zikwizikwi a m’dziko lathu adafa chifukwa cha
chifuwa.

Mnyamata wang’ono, dzina lake Mphatso
adayenera kusonkhezera moto mu mbaula ya banja lake.

Mphatso adayenera kuphika nsima ndiponso phala.

Adayeneranso kuchapa zovala,

kusesa ndi kukolopa m’nyumba

komanso kuweta ziweto zonse za Mayi wake.

Mayi wake wa Mphatso adali mayi wamasiye ndipo

adadwala chifukwa cha chifuwacho.



Achemwali ake asanu
adapatsirananso
chifuwa ndipo onsewa
adadwala kwambiri.”

“Mphatso adanyowetsa nsanza ndi kuika pa mphuni ya mayi wake kuti kutentha kwa thupi kuchepeko. Adatumikira achemwali ake mwakuwamwetsa madzi ndi phala lofewa. Garu wake wa Mphatso adafuna phala ndi msuzi. Nkhuku ndi abakha zidangomutsatira nthawi zonse akapezeka pa bwalo. Timbuzi tamasiye tidafunika kusamalika mwapadera. Nthawi zonse mbuzi zidamva njala. Abulu omwe adasowa udzu ndi madzi.”



"Agogo aamuna adamutsimikizira Sami, nati: "ndikuuze Sami, Mphatso adagwira ntchito yaikulu, chimodzimodzi anthu akuluakulu asanu ndi mmodzi. Mphatso adasisita ziweto zomva njala. 'Tontholani nonsenu. Ndikusamalani. 'Tontholani, mwamva?"

Ziweto zidafatsa pamene Mphatso adazitonthoza ndi chikondi.

Zidamudalira.

Mphatso adadyetsa chiweto china chiri chonse.

Mphatso adadziwa dzina la chiweto chiri chonse ndipo adazisamalira bwino."



“Koma Sami, mnyamata wanga, usiku wina kudazizira kwambiri.

Usikuwo udali wovuta ndi woipa.

Mayi wake ndi achemweli a Mphatso adatsokomola mosalekeza.

M’nyumba monse mudamveka fungo la kutentha kwa thupi.”



“Mwezi udabisala.

Udalowa kuseri kwa mitambo.

Chiri chonse chidazizidwa komanso kuda bii.

Mphatso adaturuka kunja kukadzitsimikizira mmene
ziweto zidaliri.

Si zonse zimene zidali bwino. Zina zidavutika.

Kambuzi kakang’ono kamodzi kadakongwa ndi
chisanu.

Mphatso adakapfundika chofunda kambuzi kaja nakhala
nako pafupi ndi mbaula.

Adakafungatira kambuziko ndikumafikisafikisa

miyendo yake

ndikumakasisita pa

msana

pake. Patapita

nthawi, kambuzi

kaja kadadzutsa

mutu wake ndi

kulirako.”





“Mphatso adathila mkaka wa mbuzi m’botolo
koma kambuziko kadakana kumwa mkakawo.
Pakhozi pake padafookanso.
Makala a m’mbaula adatheratu.

Nyale ya pa thebulo, idayambanso kuchepa mphamvu.
Ndipo kenaka, Sami, mnyamata wanga, nyale ija
idazimiratu
ndipo Mphatso wochepe adakhala mumdima wa bii.
Mphatso adayamba kulira.
Adalira chifukwa cha kudwala kwa mayi wake
ndi achemwali ake
adaliranso chifukwa cha kambuzi kofooka
ndi phulusa lopanda moto
adalira chifukwa muuni womulimbikitsa wa nyale,
udazimanso.
Mphatso adakhetsa misozi chifukwa adaunguluma
ndiponso adachita mantha.
Mphatso adaiwaliratu kuti Mulungu Atate amathandiza
ana ake,
makamaka akachita mantha
makamaka akaunguluma,
ndi pamene zinthu zikavutitsitsa.
Sami, mnyamata wanga, Mphatso adayiwala mmene
Mulungu amakondera ana.”

“Nthawi yomweyo Mphatso adakweza maso ndipo adawona mnyamata wonyamula nyale ndi kulowa pakhomo.

Mnyamatayo adafunsa ‘Kodi kambuzika kavutikiranji?’

Mwatsatanetsatane Mphatso adamufotokozerazonse.

Mnyamatayo adaika nyale yake pa thebulo.

Kuunika kudasintha zinthu zonse.

Mnyamatayo adamwetulila nati:

‘Undilole kuti ndikuphunzitse njira ziwiri za luso zothandiza kambuzi kolephera kumwera mkaka mu botolo.

Kodi ndikhoza kubwereka nsaruyi?’ Mnyamata uja adapinda nsaru ija kawiri.

Adamuza Mphatso:

‘Mnzanga, ndipatse botolo.

Chonde, phimba kumaso kwake kwa kambuzi ndi nsaruyi.’

Mnyamata uja adagwira botolo pafupi ndi mphuno ya kambuzi kaja.

Adagwedeza mutu nayang’ana kwa Mphatso nati, ‘Tsopano kafwenkha mkaka’.

‘Menya pang’onopang’ono zedi pa mchira wa kambuzi.

Mobwerezabwereza.’

Mphatso sadazindikire chifukwa choti azipitirira kukamenya pang’onopang’ono zedi pa mchira.

Mnyamata uja adamuthandiza kuti amvetsetse.



“Mayi wake wa kambuzi amamenya pang’onopang’ono zedi pa mchira wa kamwana kake. Kamwana kambuzi kamamva kutetezeka. Katatetezeka kamagwira bele la mayi wake ndi kuyamwa mkaka wa mayi wake.’ Kamwana ka mbuzi ka Mphatso kadadzutsa mutu wake. Kadafuna mkaka! Mnyamata adakalola kambuziko kuti kayamwe pa chala chake.

‘Mnyamata adamuza Mphatso, kuti ‘Kazolowera, kakhoza kuyamwa tsopano’. Moyamikira kambuzi adakalimbikitsa nati, ‘Nali, botolo la mkaka lako. Imwa mokwanira mmene ungafunire.’ Mphatso adayamba kuchotsa nsaru ija koma mnyamata adamuletsa:

‘Iyayi. Kambuzi kayenera kuganizirabe kuti kakadali pansu pafupi ndi mimba ya mayi wake. Pamenepo mpofewa ndiponso pamakhala kayaziyazi.

Bapitirira kumenya pang’onopang’ono pa mchira wake, wamva?’ Kambuzi kadakhuta. Nthawi yomweyo kadagona. Mphatso adakagoneka pa mtsamilo.”

Agogo aamuna adamusuntha Sami kuti akhale pa bondo lina la agogo wake. Ndipo adapitirira kufotokozera nkhaniyi:





“Kambuzi katadekhadi m’tulo tofa nato
Mphatso adamuza mnyamatayo, nati:
‘Ndiwe ngwazi yanga. Ndiribe mawu. Ndiwe
wochenjeradi!’



“Mnyamata adaoneka
wododometsedwa.

“Ine sindine ngwazi.
Ndine mbusa chabe.
Nanga iweyo?”

“Mphatso adamuyankha
mwatimanyazi, ‘Ineyo
ndikadakhumba

ndikadakhala mbusa wa mbuzi, monga iweyo,’

‘Komabe ndiyenera ndiyambe ndamariza maphunziro a
sukulu.’

Mnyamata adamwetulira: ‘Kodi dzina lako, ndiwe yani
mnyamata?’

‘Mphatso. Koma aphunzitsi amanditcha Mpha.’

Mnyamata uja adamwetuliranso. ‘Ine ndine Davide.

Ndiri ndi abale ndi alongo anga akulu.

Ine ndine mzime, mwana womariza m’banja la makolo
athu.

Kodi iweyo uli ndi abale ndi alongo, Mphatso?’

Mphatso adaganizira za mayi wake ndi achemwali ake
odwala aja. ‘Inde, ndiri nawo achemwali asanu. Mayi
wanganso alipo. Koma onsewa akudwala kwambiri.’”



Mkati mwa nkhaniyi

Agogo aamuna wa Sami adalandira kapu ya tiyi.

Sami adalalaka akadamva nkhani yonse, koma adadikira mwaulemu kuti Agogo aamuna amalize kumwa tiyi wao.

Agogo aakazi adafika kudzatenga kapu ya tiyi ija.

Agogo aamuna adamufunsa Sami, ‘Kodi ndinalekezera pati?’

‘Agogo, mudalekezera pamene Mphatso amamuza Davide

kuti onse a m’banja lake adalikudwala.’

‘Walondola,’ adamuyankha Agogo aamuna wa Sami.

‘Zikomo kwambiri, Sami.

Tsopano ukumva za malo

amene Davide adaopa kwambiri.’

Agogo aamuna wa Sami, adayambanso kufotokozero
nkhani ija:

“Zonse zinali bwino ndi kamwana ka mbuzi. Kakadali
m’tulo pa mtsamilo.

Davide adatambalala naye Mphatso.

Davide adamufunsa Mphatso funso lomwelo

katatu konse mondondoza:

‘Kodi uli bwino, mnzanga?’

‘Kodi uli bwino,
mnzanga wang’ono?’

‘Kodi uli bwino,
mnzanga wokondeka
wachichepere iwe?’”

Mphatso adayamba
kulira kwambiri.

‘Sindiri bwino! Ndiri
ndi mantha ndipo
ndaunguluma.’”





Davide adagwira dzanja la Mphatso:

‘Mnzanga, nthawi zina inenso ndimamva mmene wafotokozera.’

Mphatso sadamukhulupirire.

‘Koma Davide, ndiwe wochenjera! Umadziwa zonse!’

Davide adayankha, ‘Iyayi, sindidziwa zonse.’

‘Mwa nthawi yaitalidi sindinadziwe
mmene ndingalekeretu kunthunthumira ndi
kunjenjera.

Kodi kukhala wochenjera umakhala wotere?’

Mphatso adamuyang’ana Davide. ‘Kodi Davide, ndi
chiyani chimene chidakunthunthumilitsa ndi
kukunjenjeretsa?’

Davide adamunong’onezera Mphatso chinsinsi chake:

‘Ndimanthunthumila ndi kunjenjera ndikamachita
mantha.’

Atatero Davide, adamufotokozera za umo amakhalira
ku tchire.

‘Nthawi zonse ndimayesetsa kusamalira mbusi za
Bambo wanga kuti zikhale ndi chakudya chokwanira.
Tiana ta mbuzi tiyenera kupeza udzu wanthete.

Ndimazitsogolera ku udzuwo.

‘Ndimazitsogolera ku malo opezeka madzi oyera.
Mphatso, mbuzi zathu zimamwa madzi abwino ku
maloko.’



“Mбузи zathu zikatopa zikafuna kupumapo,
ndimangokhala nazo pomwepo’.

Adani ake monga afisi ndi mikango zimapezeka pafupi
ndi mbuzizo:

Zimafunafuna kuzigwira mbuzi.’

Mphatso adachita chidwi, adamufunsa Davide, ‘Nanga
umatani kuzisamalira ndi kuzitetezera?’

Davide adayankha momveka kuti, ‘mkango ukafika
ndikugwira kamwana ka mbuzi pakati pa zinzake,
ndimaulondola

ndikukalanditsa kambuziko.’

‘Nthawi zina ndimaugwira mkangowo ndikuupha.’

Mphatso adadabwiratu. Adasowa cholankhula.

Kenaka adalankhula, nati:

‘Davide ndiwe wopanda mantha!

Palibe chiri chonse chimene chikhoza

kukunthunthumiritsa ndi kukunjenjemeretsa!’”



Poyamba kufotokozerwa gawo lina la nkhaniyi,

Agogo aamuna wa Sami adamgwira momufungatira.

“Sami, Mphatso sanayerekeze bwino.

Chimenechi wachidziwa. Wina ali yense amaopsedwa
ndi china chake.

Sami wavomera. “Agogo aamuna, ndimanjenjemera
ndipo ndimanthunthumila kwambiri.

Ndimachita mantha ndi mphezi. Ngakhale jekeseni.

Ndiponso tizirombo ta ululu.”

Agogo aamuna adamuyankha, “Agogo aakazi wako
amachita mantha ndi zifukufuku!”

Sami ndi Agogo aamuna adaseka limodzi.

Agogo aamuna wake adapitiriranso kufotokozerwa
nkhaniyo:

“Davide adamufotokozerwa Mphatso chomwe adaopa
koposa china chiri chonse.

Kodi Sami, iweyo ukuganiza kuti Davide adaopa
chiyani?”

Sami sadadziwe ndi pang'onong'ono pomwe kuti chitha
kukhala chiyani.

“Agogo aamuna, kodi Davide adaopa chiyani?”



“Davide adamufotokezera kuti adaopa chigwa cha mthunzi wa mdima.

Kawirikawiri adayenera kutsogolera mbuzi modzera m’ malo a mdima ndiponso moopsya.”

Davide adamuuza Mphatso: ‘Mnzanga, m’chigwa cha mdima dzuwa siliwala.

M’chigwacho ndimakhala ndekha ndipo ndimanthunthumila ndi kunjenjemera.’

Mphatso adamupangira Davide:

‘Kodi Davide chifukwa nchiyani sungadutsire njira yina potsogolera mbuzizo?

Ineyo ndikadatero ndithu.’

Davide adamuyankha: kulibe njira yina iri yonse,

‘ndiyeneradi kudzera m’chigwacho cha mdima.’

Mphatso adanena: ‘Ndikadalephera, nagonja.’”

‘Davide, nanga umapirira bwanji?’

Davide adamuuza: ‘Ndimanyamula timbuzi tofooka.

Ndimayesetsa kuyenda mofulumira.

Ndimamenya thanthwe ndi ndodo.

Ndimapemphera, Mphatso. Ndimapempha kwa

Ambuye Mulungu.’”

Mphatso adafunitsitsa kudziwa, motero adafunsa ‘Kodi kupemphera kumathandiza?’”



Gawo lopambana la nkhani Agogo aamuna adafotokoza
mwa luso ndiponso mokometsera monga
ngati liu la yankho la Davide likumveka bwino lomwe:

“Mphatso, wandifunsa ngati kena kake kamachitika tikapemphera.

Inde, inde, inde, Mphatso!

Mulungu AMBUYE wathu amatha kuchita koposa mmene ife timaganizira!

Tsiku lina ndiri mkati mwa kupemphera, ndidamva mawu.

Wina adandiuza:

Davide, ndiwe mbusa wabwino kwambiri.

Umakonda ziweto zonse za bambo wako.

Komabe uzikumbukira:

Ineyo, AMBUYE, ndine Mbusa wako.

Ineyo, AMBUYE, ndimakukonda koposa mmene iweyo umakondera mbuzi zimene umazisamalira.

Ineyo, AMBUYE, ndimakuyang'anira.

Ndimakuteteza koposa mmene umatetezera tiana ta mbuzi timene umatisamalira.

“Kuunika kwa AMBUYE Mulungu

kudawala m'chigwa cha mdimacho.

Mawu a AMBUYE Mulungu

adaletseratu kunthunthumila ndi kunjenjemera konse.



AMBUYE Mulungu adanena:

Davide, umasamala kuti ziweto zako zikhale nazo zofunika zonse za pa moyo wake.

Ine, AMBUYE, ndidzakuchitira koposa.

Davide umatsogolera mbuzi zako ku msipu wobiliwira ndi ku zitsime za madzi abwino.

Ukamakhala pafupi ndi mbuzi zako, siziopa chiri chonse.

Koma Davide, Ineyo, AMBUYE, ndidzakupatsa zinthu zina zabwino zoposa udzu wobiliwira ndi madzi opezeka mu zitsime.

Ine ndine Mulungu. Ine ndiri nawe.

Suyenera kuopa china chiri chonse.

Ine, AMBUYE, ndidzakutsogolera nthawi zonse.

Davide, ukaopsedwa,

ukhoza kundidalira koposa

mmene ziweto zako zimakudalilira.

Davide, Ine ndine AMBUYE. Ine ndine Bwenzi lako.

Ndidzakusamalira nthawi zonse.”



Agogo aamuna wa Sami adamufotokozerawo gawo lomariza la nkhaniyo:

“Davide adanyamula nyale yake kuti abwerere kukasamala mbuzi zake.

Koma asananyamuke, adamufunsa Mphatso:

‘Mphatso, kodi umamkonda AMBUYE?’

Mphatso adayankha: ‘Ndimamkonda, ndidzamuwona m’tsogolomo.

Sinditha kumuwona tsopano, koma ndimamukonda kwambiri.’

Davide adamufungatira Mphatso.

‘Mphatso, AMBUYE ndiye Mbusa wakonso.

Iye ndiye Mbusa wamkulu wa onse amene amamukonda.

Iye ndiye Bwenzi leni leni la mwana wina ali yense amene amamupembedza.

AMBUYE Mbusa wathu amapezeka chifukwa cha ife, tsiku ndi tsiku ndiponso usiku uli wonse.

Iye ndiye Bwenzi lako la Usiku ndi Bwenzi lako la Usana womwe.’”

Agogo aamuna, adamutsitsa pa bondo lawo.
 “Sami, mnyamata wanga, Mphatso atayang’ananso,
 Davide adali atafika kale patali.
 Kanyale kake kadawonekera ngati kadontho
 kakang’ono kofiilira mumdima wa usiku.
 Mchemwali wa Mphatso adamuitana kuchokera ku
 chipinda:
 ‘Kodi Mphatso, ndamva mau a ndani?’
 Mphatso adayankha: ‘Ndi mawu a bwenzi langa la
 usiku’.
 Mayi wake wa Mphatso adayatsa nyale pafupi ndi bedi
 lawo.
 Chipinda chonse chidadzala ndi kuunika kofiirila.
 Aliyense adawoneka kuti adasinthako.
 Mphatso adawafotokozera za bwenzi lake la usiku.

Adawafotokozera za
 Davide mbusa wa
 mbuzi.
 Mphatso
 adawauzanzo za
 Ambuye Yesu
 Khristu,
 Bwenzi la onse
 amene amamukonda
 Iye.
 Mphatso adati kwa
 iwo:
 Bwenzi lathu la
 mphamvu, Yesu
 Khristu, limakhala
 nafe
 nthawi zonse, usana ndi usiku.





Agogo aamuna adamufotokozera Sami za nkhani ya
bwenzi la usiku, kutangokhala masiku awiri boma
lisanalamulire kuti pakhale nyengo yoyimitsa zochitika
za magulu chifukwa cha Covid-19.

Kwa masiku awiri okha

bwalo la msika wa malonda lisanatsekedwe

Sami ndi Agogo aamuna wake

adayimba nyimbo ya Davide:

AMBUYE, ndiye mbusa wanga;

ndiri nazo zonse zimene ndimazisowa.

Agogo aakazi, mayi wake ndi bambo wake wa Sami
adalumikizana nawo poyimba.

Nyimbo ya Davide idawasangalatsa kwambiri.

Nthawi idawathera.

Adayenera kulawirana nawo Agogo aamuna ndi Agogo
aakazi.

Koma Samiyo adalephera kuleka kuyimba.

Sami adayimbanso nyimbo ya Davide ulendo womariza:

Sami akuyimba nyimbo ya Davide.

AMBUYE ndiye Mbusa wanga.

Safuna kuleka

kuyimba.

Sami adalephera

kuyimba!



“Sami, Sami!”

Bambo wake akumuitana Sami.

“Ukuyimba bwino kwambiri, Sami
koma uyenera kudzuka tsopano.”

Sami akumva liu la mayi wake:

“Mgiligishe, Chikondi.”

Chikondi akuseka monga amaseka mwana: “Guho!
Guho!”

Sami akutsegula maso ake.

Kwacha. Kuunika kwa dzuwa kwawonekera pa zenela.

Wakhala akumvera nkhani ya Agogo aamuna
usiku wonse.

Wakhala akuyimba nyimbo m’maloto ake.

Kuwala kwa Ambuye kwakhala kuli m’maloto ake.

Kuwala kwa AMBUYE kwaposeratu
kuwala kwa dzuwa.

China chiri chonse chidali bwino
kwambiri.

AMBUYE adali pa mbali yake
Sadaungulume konse.

AMBUYE adachotseratu mantha ake
onse!





Mayi wake adati, “Dzuka, Sami!”

“Bwera undithandize kumanga dengu la katundu pa njinga.”

Sami akudzuka msanga: “Kodi Mayi, mukupita ku bwalo la msika wa malonda?”

Mayi wake akuyankha, “Iyayi”.

“Lero tiri ndi chakudya chochuruka moti ndikupita kukagawirako ena pa ulendo wanga wopita ku ntchito.”



Woyang'anira waku ntchito ya Bambo wako adapereka matumba a ufa ndi nyemba.

Bambo wako adafika ku nyumba ndi matumba ochuruka a chakudya, choti ena osowa chakudya akhoza kulandirakonso.

Mayi wa Sami sakuwonekanso wotopa.

Akusangalala kuti adapeza chakudya chothandiza osowa.



Sami adanyamula matumba ndi kupita nawo pa njinga
ya mayi wake.

Pusi akumutsatira.

Pusi akufwenkheza matumbawo

koma pfungo ndi losamkondweretsa Pusi.

Amakonda mileme.

Sami akuseka. “Patuka, Pusi!”

Akumanga dengu pa njinga ya mayi wake.

Sami akuganiza, AMBUYE ndiye Mbusa wathu.

Mwa Iye tiri nazo zonse zofunika pa moyo wathu.



Mayi wake akuti, “Tiyeni, tipemphere limodzi ndisanapite ku ntchito”.

Onse akukhala panso pa bedi la Sami,
Sami ndi Bambo wake ndi Mayi wake
pamodzi ndi Pusi ndipo Chikondi akukhala pakati pawo.

Bambo wa Sami akuthokoza AMBUYE
chifukwa chokhala Mbusa wawo Wabwino.

Sami akuti, “AMBUYE ndiyenso Bwenzi lathu la
Usiku”.

“Pamene pali AMBUYE, mantha onse amachoka.”
Akuyimba nyimbo ya Davide.
Nyimboyi ikhala ya banja lawo chikhalire:
Yesu Khristu ndiye Mbusa wanga!



Mayi wa Sami akunyamuka pa ulendo wopita kuntchito,
panjira akugawa maphukusi a ufa ndi nyemba kwa
osowa chakudya.

Bambo wa Sami akutsuka mbale.

Atamariza kutsuka mbale, akukagona.

Tulo tikumugwera mofulumira.

Chikondi akukwawa pena paliponse.

Pusi akukhala pa mpanda wa thabwa

ndipo Agogo aamuna wa Sami akuyimba foni.

Sami akuti, “Agogo aamuna,

chonde, muzisamba m’manja mwanu kawirikawiri.

Ndipo Agogo aamuna, Yesu ndiye Bwenzi lathu la

Usiku!”

MASALIMO 23: Amwai amene Yehova akhala Mbusa wao
Salimo la Davide.

1 Yehova ndiye mbusa wanga; sindidzasowa.

2 Andigonetsa kubusa lamsipu,
anditsogolera kumadzi odikha.

3 Atsitsimutsa moyo wanga;
anditsogolera m'mabande a chilungamo, chifukwa cha dzina lake.

4 Inde, ndingakhale ndiyenda m'chigwa cha mthunzi wa imfa,
sindidzaopa choipa; pakuti Inu muli ndi ine;
chibonga chanu ndi ndodo yanu, izi zindisangalatsa ine.

5 Mundiyalikira gome pamaso panga m'kuona kwa adani anga;
mwandidzoza mutu wanga mafuta; chikho changa chisefuka.

6 Inde ukoma ndi chifundo zidzanditsata
masiku onse a moyo wanga,
ndipo ndidzakhala m'nyumba ya Yehova masiku onse.

YOHANE 10:11-16: Ine [Yesu Khristu] ndine Mbusa Wabwino;
mbusa wabwino ataya moyo wake chifukwa cha
nkhosa. 12 Wolipidwa amene sakhala mbusa, amene nkhosa sizili
zake za yekha, aona mmbulu ulinkudza, nasiya nkhosazo,
nathawa; ndipo mmbulu uzikwatula, nuzibalalitsa; 13 chifukwa ali
wolipidwa, ndipo sasamala nkhosa. 14 Ine ndine Mbusa
Wabwino; ndipo ndizindikira zanga, ndi zanga zindizindikira
Ine, 15 monga Atate andidziwa Ine, ndi Ine ndimdziwa Atate;
ndipo nditaya moyo wanga chifukwa cha nkhosa. 16 Ndipo
nkhosa zina ndili nazo, zimene sizili za khola ili; izinso ndiyenera
kuzitenga, ndipo zidzamva mau anga; ndipo zidzakhala gulu
limodzi, mbusa mmodzi.

